NYA_TTB_1099_SCRIPT

1 Yohane : 2

Mutu : Wokhulupirira ayenera kumdziwa Kristu

Ndipereka moni wa Kumwamba kwa inu wokondedwa anzanga apaulendo. Lero Ambuye atitsogolere ndi mau apa Amosi 3:7, amene akuti, “Pakuti Ambuye Yehova sadzachita kanthu osaulula chinsinsi chake kwa atumiki ake aneneri.”

Tsono mupologalamu yatha tinali kusanthula 1 Yohane 2:23-29, pamene timakambirana nkhani ya kumdziwa Yesu Kristu. Ndipo lero pa 1 Yohane 2, tipitiliza kuona nkhani yakuti wokhulupirira ayenera kum’dziwa Kristu.

Pologalamu ino, iona kwambiri maphunziro osiyana-siyana amene tikuwapeza mu 1 Yohane 2. Ndiye poyamba pamene tinena kuti mkristu amdziwa Yesu Kristu, ndiye kuti ayenera kukhala ndi chidziwitso chokwanira cha Iye.

2. Ndipo Iye ndiye chiombolo cha machimo athu; koma wosati athu okha, komanso a dziko lonse lapansi.

Yohane pano akunena kuti ngati munthu wokhulupirira achita tchimo, ali ndi Nkhoswe kwa Atate. Kunena kuti nthawi yomwe wachitayo kapena nthawi yomwe walankhula mau oipa, Ambuye Yesu ali kale pampando wachifumu wa Mulungu kutiimira ife monga momwe amachita satana kutineneza.Ndiye chimene chimachitika ndi chakuti pamene Ambuye Yesu apereka pembedzero lake lokhulupirika kwa Atate, nthawi yomweyo Mzimu Woyera amadza ndi kutitsutsa, kotero kuti timabvomereza tchimolo kwa Atate.

Wokondedwa anzanga apaulendo, apa ndipo pamene mwana wokhulupirika wa Mulungu amafunitsitsa kukondweretsa Atate nthawi yonse. Tikunena kuti inu ngati mwana wa Mulungu muyenera kutsimikiza mtima wanu kuti mwachitadi choipa, osati mukakamizidwe ayi. Kutanthauza kuti chiyanjano chanu chimabwezeretsedwa pamene mubvomereza tchimo lanu pamaso pa Mulungu.Tere, mukhoza kuona kuti Yohane afuna kuti aonetse kuti inu muli m'banja la Mulungu momwe Iye afuna kukhala m'chiyanjano ndi inu.Kodi inu muli wokonzeka kumuuza Mulungu chofoka ndi cholakwa chanu?

3. Ndipo umo tizindikira kuti tamzindikira Iye, ngati tisunga malamulo ake.

Ndiye poyamba ndifuna ndinene kuti ndime tawerengayi, si-ikukamba za chitetezo cha mkristu, koma ikukamba za chitsimikizo. Tikuti ife tonse ndife a m'banja la Mulungu. Kodi tingatsimikize bwanji kuti tiri m'banja la Mulungu?Yohane akuyankha kuti chitsimikizo chathu chili pakumvera ndi kusunga malamulo ake.

Ichi, ndichimene akunena kuti, "Ngati tisunga malamulo ake." Koma sakunena malamulo khumi a Mose ayi, popeza aja akukhudza mtundu wa Israyeli komanso mitundu ina. Yohane akunena kuti pokhala tsopano Mulungu ali ndi banja lake, ayenera apereke malamulo okhudza ana akewo. Kutsindika kuti malamulo khumi amaimira anthu akunja, amene sali m'banja la Mulungu, anthu amene asanapulumutsidwe. Tamvani pa Agalatiya 6:2, Mulungu kudzera mwa Mtumwi Paulo akuuza ana ake kuti, "Nyamulirananizothodwetsa, ndipo kotero mufitse chilamulo cha Kristu." Komanso Paulo pa 1 Atesalonika 4:2, akuuzanso banja la Mulungu kuti, "Pakuti mudziwa malangizo amene

tinakupatsanimwa Ambuye Yesu.”Tere malamulo omwe akupezeka kumapeto a 1 Atesalonika ndiwo okwanira 22 ndipo pano malamulo ena akuti, “Kondwerani kosalekeza.”Kutanthauza kuti Mulungu afuna inu ndi ine, kuti tikhale ana wokondwa nthawi yonse.Komanso tamvani akunena kuti “pempheranikosaleka.”Mulungu afuna ana ake onse akhale m’moyo wopemphera nthawi yonse.Komanso akunena kuti “MusazimitseMzimuyo.” Kutanthauza kuti inu simuyenerakuukaniza Mzimu wa Mulungu pamene ukukudzudzulani, kukuunikirani ngakhale kukulangizani kumene. Mwanjira ina inu simuyenerakufoketsa Mzimu wa Mulungu pa inu.

Wokondedwa anzanga apaulendo, awa ndi malamulo ena amene Ambuye Yesu adaperekakwa wokhulupirira onse ndi cholinga chakuti akhale ndi chitsimikizo ndi chisangalalo pamene akhala m’chiyanjano cha Atate mwakusunga malamulo amenewa. Kutsimikiza kuti ngakhale inu ndi ine, tidamasulidwa ku gori la satana, koma tiri m’banja la Mulungu momwe muli malamulo ake, kotero kuti sitiriwomasuka kuchita chomwe ifetifuna ayi. Koma

akristu ayenera kuchita chomwe chikomera Ambuye wawo, Yesu Kristu.

15. Musakonde dziko lapansi, kapena za m'dziko lapansi. Ngati wina akonda dziko lapansi, chikondi cha Atate sichiri mwa iye.

Tsono pamene Yohane akunena kuti "Musakonde dziko lapansi, kapena za m'dziko lapansi," kodi dziko lomwe iye akunena ndilo liti?Apa, ndipofunika kumvetsa bwino, popeza iye sakunena dziko lomwe lidalengedwali, koma akunena momwe anthu akuyendetsera ulamuliro m'dziko lino. Tikunena kuti sakulankhula za dziko lomwe Mulungu adalenga momwe tiona zinthu zochuluka zolengedwa ayi.Tikaona dziko lomwe Mulungu adalenga, tipeza kuti zinthu zikuchitika monga momwe adakhazikitsira.Taonani kuti m'nyengo yake timaona maluwa komanso masamba amaoneka pamitengo.Ndipo pakutha panyengo imeneyi, masambaamagwa ndipo nyengo yoziziraimayamba.Ili, si dziko lomwe tikulinenali ayi. Tikunenetsa kuti dziko ili, Mulungu adalilenga ndi cholinga chakuti inu ndi ine, tikhalemo ndi kukondwamo.

Tsono mwina inu mukufunsa kuti, kodi Yohaneyu akunena za anthu omwe ali pa Yohane 3:16, pamene akuti, “Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero kuti anapatsa Mwana wake Wobadwa yekha, kuti yense wakukhulupirira Iye asataike, koma akhale nawo moyo wosatha?” Ayi, ili, sidziko lomwe Yohane akunena mundime yomwe tawerenga ija. Yohane akunena za dziko lomwe lilikulamulidwa ndi satana kapena dziko lomwe lili muulamuliro wa satana, lomwe likutsutsana ndi ulamuliro wa Mulungu. Tere ili, ndidziko lomweife, sitiyenera kuyanjananalo popeza litsutsana ndi Mulungu.

Ndifuna kunenetsa pano kuti m’dziko lapansi muli ulamuliro wa satana womwe ndiwotsutsana ndi Mulungu. Ndikunena mau amenewa chifukwa Ambuye Yesu pa Yohane 14:30, akunena mau akuti, “Sindidzalankhulanso zambiri za inu, pakuti mkuru wa dziko lapansi adza; ndipo alibe kanthu mwa Ine.” Ndiye “mkuru wa dziko lapansi” amene akumunenayu ndiye satana, amene akulamulira dziko lino m’zochitika zonse. Tikunena kuti ulamuliro wonse wa dziko lapansi uli m’manja mwake. Mukumbukira kuti ndiye uja anapereka mwayi kwa Ambuye Yesu kuti akamugwadira,

adzampatsa ulamuliro wa dziko lapansi pamene anali kukayesedwa. Pachifukwa chimenechi ine, sindikhulupirira kuti dziko lathu la Malawi linapatulidwa ayi. Kutsimikiza kuti dziko lathuli lilimuulamulirowa satana popeza Ambuye Yesu adanena kuti samayenera kumgwadira iye, koma Ambuye Mulungu wathu ndiye. Tamvani pa Yohane 16:11, Ambuye Yesu akunena kuti, “Za chiweruziro, chifukwa mkuru wa dziko ili lapansi waweruzidwa.” Kutsimikiza kuti inu simuyenera kutsatira ulamuliro wa satana popeza ndiwo umene unaweruzidwa kale kuti ukupitakuchilango.

Tsono Paulo pa Aefeso 1:4, akunena kuti, “Monga anatisankha ife mwa Iye, lisanakhazikike dziko lapansi.” Kunena kuti Mulungu anatisankhaifelisanakhakike dziko lino pachuma kapena pazinthu zooneka ndi maso. Ndiye Paulo pa Aefeso 2:2, anati, “Zimene munayendamo kale, monga mwa mayendedwe a dziko lapansi lino, monga mwa mkuru wa ulamuliro wa mlengalenga, wa Mzimu wakuchita tsopano mwa ana a kusamvera.” Apa anali kuwakumbutsa akristu aku Aefeso kuti kale iwowa anali kuyenda monga mwakayendetsedwekadziko lapansi. Kutanthauza kuti iwowa anali ndi mtima wodzala ndi dyera, kudzikonda ndi

zilakolakozathupi, zachinyengo ndi zoopsa.Ili, ndilo dziko lomwe tikukhalamo lero, tere Yohane akunena kuti, inu ndi ine, sitiyenera kulikonda dziko limeneli. Chitsimikizo chilipo chakuti inu ndi ine, tikukhala m'dziko loukira Mulungu, kotero kuti ife sitiyenera kukonda dziko limeneli. Tsono mukaona miyambo ndi makhalidweathu, zonsezi ndizoukira Mulungu ndipo mwana wa Mulungu sayenera kukonda dziko limeneli. Tikunena kuti inu ndi ine, tiyenera kumachita nawo komanso kumagwira nawo ntchito za dziko, koma sitiyenera kuchita monga anthu adziko ayi.

Chinthu chimene muyenera kudziwa ndi chakuti inu, muyenera kukhala womvera ku ulamuliro umodzi panthawi yake. Kutanthauza kuti inu muyenera kukhala womvera ulamuliro wa dziko lino, ndi kukhala mwamtendere ndi chisangalalo kapena kusankha kumvera Mulungu. Ndiye Paulo pa Agalatiya 6:14, akuti, "Koma kudzitamandira ine konse konse, iyayi, koma mu mtandawa Ambuye wathu Yesu Kristu, amene mwa Iye dziko lapansi lapachikidwira ine, ndi ine ndapachikidwira dziko lapansi." Paulo akutanthauza kuti dziko lapansi likuyembekeza iye, koma iye ngati mwana wa Mulungu ayenera kukhala womvera Iye ndipo ali

womvera Iye ndi kukondwera mu mtanda wa Kristu. Kodi inu mukaona dziko lapansili, likuonetsa kukondwera mu mtandawa Kristu kapena mu ntchito yomwe Kristu anagwira?

20. Ndipo inu muli nako kudzoza kochokerakwaWoyerayo, ndipo mudziwa zonse.

Mtumwi Yohane pano akunena za kudzoza kwa Mzimu Woyera. Iye akuti, wokhulupirira aliyense akadzakwa Ambuye ndi kupereka moyo wake kwa Iye, amalandira kudzoza kwa Mzimu wa Mulungu nthawi yomweyo. Ndiye Mzimu uyu, ndiye amakhala mwa munthu wokhulupirira weni-weni nthawi zonse, kotero kuti Mzimuyuamamuululira zinthu zonse zomwe Ambuye afuna kuti azidziwe. Ichi, ndichimene Paulo akunena pa 1 Akorinto 2:9-10, pamene akuti, “Koma monga kulembedwa, zimene disosilinaziona, ndi khutu silinazimva, nisizinalowa mu mtima wa munthu, zimene ziri zonse Mulungu anakonzeratu iwo akumkonda Iye. Koma kwa ife Mulungu anationetsera izi mwa Mzimu; pakuti mzimuasanthula zonse, zakuya za Mulungu zomwe.” Kutsindika kunena kuti Mulungu adaika Mzimu Woyera mumtima mwathu kuti azitiululira zinthu zomwe ziri m’mau a Mulungu.Tere kudzoza kumene inu ndi

ine tiri nako, ndiko kumene kumapangitsa kuti titsimikize za chipulumutso chathu ndipo pamene inu mufuna kukhala m'chiyanjano ndi Mulungu, muyenera kudza kwake ndi kupempha uphungu ndi chitsimikizo chake.

Ndiye pamene Yohane akunena kuti, "ndipo mudziwa zonse," akunena kuti inu ngati mwana wa Mulungu muli ndi kuthekera kuzindikira zinthu zonse zomwe Mulungu afuna kuti inu muzidziwe. Koma ndikofunika kumvetsa chifukwa anthu ambiri amanena kuti safunika kuphunzira mau a Mulungu popeza Mzimu Woyera amaulula zonse.Tamvani wokondedwa, izi ndizoona ndithu koma sizitanthauza kuti Mzimuyoamangothira mumtima mwanu zisinsizo ayi, koma kuti amagwiritsa ntchito njira yoyenera yakuphunzira ndi kusanthula mau a Mulungu.

Wokondedwa anzanga apaulendo, ndifuna kunenetsa kuti akristu onse ndiwo amene amaphunzitsidwa ndi Mzimu wa Mulungu ndipo kuti amazindikira zomwe chipembedzo choyenera chifuna ndipo kuti asagwem'chiphunzitso choipa. Ndiye monga mwatanthauzo la ndime imeneyi ndifuna tiphunzire kuti; akristu ndiwo anthu amene amaunikiridwa ndi kuphunzitsidwa ndi Mzimu Woyera m'zinthu

zonse zauzimu. Pachifukwa chimenechi, tikunena kuti iwo amene anadzozedwa ndi Mulungu mwa Kristu, alinayo mphamvu yonkaniza satana, kukanizaaneneri wonyenga, amene afuna kuwalekanitsa ndi Atate komanso ndi Ambuye Yesu Kristu. Ndiye tikunena kuti wokhulupirira aliyense ali ndi Mzimu wochokera kwa Mulungu komanso kwa Mwana wake. Tere Mzimu Woyera ndiye chizindikiro chakuti ife tikhala mwa Atate ndi mwa Mwana wake Yesu Kristu.

Tsono mafuta omwe amathiridwa pamutu pa ansembe ndi mafumu, ndiwo chindikiro chomwe chimaimira kuti mafuta auzimuamachokerakwa Kristu kudza kwa ife. Kutsimikiza kuti inu ndi ine, sitingakhale akristu oona popanda Mzimu wa Kristu. Tere tiyenera kukhala mwaKristu monga Kristu analandira unsembe kuchokera kwa Atate.

Ndiye pamau akuti, “Ndipo mudziwa zonse” akutanthauzanso kuti maganizo a mkristu amakhala ndi chidziwitso cha choonadi. Munthu wokhulupirirayu tsopano amaona mkuwala kusiyana ndi kale.Iyeyu amakhala ndi chidziwitso chabwino cha chikhulupiriro cha chipembedzo chake kusiyana ndimomwe amaonera

kale.Kunena kuti chinthu chomwe samaonetsetseka, tsopano chimaoneka mwangwiro komanso chokongola.Chinthu chimene chinali chosakongola kale, tsopano chimaoneka chokongola ndi chomtenga-mtima munthu wokhulupirirayu. Yohane akutsindika kunena kuti ife wokhulupirira timaona choona mkuunika kotero kuti sitikayika konse kuti ndicho choonadi. Pachifukwa chimenechi, mkristu amalimba mtima ndipo safuna kumva zina kotero kuti amakhala wodzipereka ngakhale kutaya moyo wake chifukwa cha choonachi.

Tsono Yohane amalemba mau amenewa ndi cholinga chofuna kulimbikitsa akristu ndi wokhulupirira ena onse, m'nyengo yoopsya kuti akhale wokhazikika m'nthawi ya ziphunzitso zokana Kristu.Kodi ndinu m'modzi mwa akristu wokhazikika m'chiphunzitso cha chipembedzo choona?

23. Yense wakukana Mwana alibe Atate; wobvomereza Mwana ali ndi Atatenso.

Tiyeni pano tiyambe ndi mau akuti pamene inu munena kuti mumakhulupirira Mulungu, koma mukana umulungu wa Kristu, zikutanthauza kuti inu simukhulupirira mwa Mulungu, wa

m'Baibulo. Ndikunena mau amenewa chifukwa Mulungu wa m'Baibulo ndiye amene adatuma Mwana wake m'dziko lino kudzafera machimo anu ndi anga. Ndiye popeza Mwana ndiye Mulungu amene, kotero kuti ndi yekhayo amene akanapereka nsembe yokwanirakwa Mulungu chifukwa cha machimo athu. Pachifukwa chimenechi tikunenetsa kuti "mzimu uli wonse umene ubvomereza kuti Yesu Kristu anadza m'thupi, uchokera mwa Mulungu; ndipo mzimu uli wonse umene subvomereza Yesu suchokerakwa Mulungu; ndipo uwu ndiwo mzimu wa wokana Kristu umene mudamva kuti ukudza; ndipo ulimo m'dziko lapansi tsopano lomwe" (1 Yohane 4:2-3). Tere tikunena kuti Yesu akanakhala munthu wina osakhala Mulungu ndiye kuti akanakhala wochimwa. Ndiye monga pali m'gwirizano weni-weni pakati pa Atate ndi Mwana, zikutanthauza kuti sipangakhalenso kutsutsana m'chiphunzitso ndi m'chidziwitso. Kutanthauza kuti pamene inu muli ndi chidziwitso choona cha Mwana, muli ndi chidziwitso choona cha Atate.Apa, ndipo pamene inu mungakhale ndi bvumbulutso kapena chidziwitso choona cha chikristu chanu.

29. Ngati mudziwa kuti ali wolungama, muzindikira kuti ali yensenso wakuchita chilungamo abadwa kuchokera mwa Iye.

Tsono pamene Mtumwi Yohane akuyamba ndime iyi ndi liwu lakuti “Ngati” sakunena kuti pali kukaikira za chiyero cha Kristu ayi. Koma akungofunakukumbutsa wokhulupirira kuti ndichinthu chodziwika kale kuti Kristu ndiye woyera. Mwanjira ina akunena kuti munthu aliyense amene ali m’chiyanjano choona ndi Kristu ayenera kukhala ndi chitsimikizo chakuti Kristu ndiye wolungama. Ndiye akunena kuti,kuti wokhulupirira onse amene atsimikizadi kuti ndiwo alim’chiyanjano ndi Kristu wolungamayu, ayenera kuzindikira kuti ndiwo amene anabadwanso mwa Kristu. Mwanjira ina Mtumwi Yohane akunena kuti inu (wokhulupirira) mukudziwa kuti Mulungu ndiye wolungama pachifukwa chimenechi, muyenera kuzindikira kuti zotsatira zakuti munthu aliyense woyendam’chiyero cha Mulungu, nayenso akhala wolungama. Kutsimikiza kuti munthu ameneyu ndiye amene anabadwanso mwa Mulungu.Kutanthauza kuti chinthu choyerachimaturutsa kapena chimabalachoyera. Mwa mau amenewa tikunena kuti Mulungu ndiye woyera kotero kuti ndiye kasupewachiyero chonse. Ndiye

popeza Mulungu ndiye chitsime cha chiyero cha munthu, zikutanthauza kuti munthuyu anapeza chiyerochi mwanjira yakubadwanso mwa Mulungu.

Wokondedwa anzanga apaulendo, tiyeni titsirize ndi mau akuti, uwu ndiwo umboni wokwanira umene udzaonetsa nthawi zonse kuti inu ndinu mwana wa Mulungu. Mwa mau onsewa, Yohane akunena kuti ana a Mulungu amaoneka ngati Atate awo.Ndiye ngati anawosangafanane ndi Atate awo, ndiye kuti si ana Atatewo.Kodi inu muli ndi chitsimikizo chakuti ndinu mwana wofanana ndi Atate anu?

Kwalerotilekeza pano.Ndipo timasanthula 1 Yohane 2, pamene timaona kuti mkristu ayenera kumdziwa Kristu.

Ambuye akudalitseni inu lero. Amen!